

KUTHANA NDI APHUNZITSI ABODZA

Phunziro 12 September 19, 2026



“Pakuti zida zathu zankhondo si
zida za dziko lapansi. Koma ndi
mphamvu zochokera kwa Mulungu
zotha kugwetsa malinga.”


(2 Akorinto 10:4, CCL)



Paulo anadzipereka kuti azidziwa nthawi zonse mmene mipingo yonse ikuyendera. Chifukwa chiyani? Kuti adziwe ngati ankafunika thandizo lililonse, kuchezeredwa, chitonthozo, kapena mawu olimbikitsa (2 Akorinto 11:28).

Nthawi zina ankauzidwa za aphunzitsi onyenga omwe ankachititsa anthu okhulupirika kutaya chikhulupiliro chawo. Zimenezi zikachitika, mtumwiyu ankadzazidwa ndi mkwiyo (2 Akorinto 11:29).

Kumapeto kwa kalata yake yachiwiri yopita kwa Akorinto, Paulo akufotokoza za vuto la aphunzitsi onyengawa. Kodi tingawazindikire bwanji? Kodi tingalimbane nawo bwanji pankhondo yauzimu imeneyi? Kodi tingawagonjetse bwanji?



Nkhondo yauzimu:

- Zida zankhondo (2 Akorinto 10:1-11)
- Njira yoyenera yodzitchinjirizira (2 Akorinto 10:12-18)



Mmene tingachitire ndi aphunzitsi onyenga:

- Onyenga odziyesa kukhala atumwi (2 Akorinto 11:1-15)
- Paulo ndi aphunzitsi onyenga (2 Akorinto 11:16-31)
- Kudzifufuza ndi chigonjetso (2 Akorinto 12:14-13:10)

NKHONDO YAUZIMU





ZIDA ZANKHONDO


"Pakuti zida zathu zankhondo si zida za dziko lapansi. Koma ndi mphamvu zochokera kwa Mulungu zotha kugwetsa malinga." (2 Akorinto 10:4)



Paulo ankaimbidwa mlandu wokhala wamantha komanso wosachita zinthu mwaluso pamaso pa anthu, ngakhale kuti ankalankhula mwamphamvu m'makalata ake (2 Akorinto 10:10).

Poyankha mlandu umenewu, Paulo anafotokoza momveka bwino kuti akanatha kulankhula mwamphamvu atakumana maso ndi maso ndi anthu monga momwe ankachitira polemba makalata ake, koma kuti samafuna kutsitsa mlingo wake ndikugwiritsa ntchito "zida za thupi" (monga ulamuliro wa nkhanza, zilango zakuthupi, kapena kudzitamandira), m'malo mwake ankagwiritsa ntchito zida "zamphamvu mwa Mulungu" (2 Akorinto 10:2-4).

"Zida" zimenezi zikuphatikizapo kuchita zinthu modzichepetsa ndi mofatsa monga Khristu (Mateyu 11:29). Koma zikuphatikizaponso kuima njii polimbana ndi zolakwika, monga mmene Yesu anachitira (Mateyu 21:12-13), kapena kulankhula momveka bwino pamene pakufunika kutero (Mateyu 23:23-27).



Ulamuliro wa Paulo unapatsidwa kwa iye ndi Khristu, ndipo nthawi zonse ankaugwiritsa ntchito pomangirira ena, osati powaononga (2 Akorinto 10:8).

NJIRA YOYENERA YODZITETEZERA

"Pakuti munthu amene amavomerezedwa, si amene amadziyenereza yekha, koma munthu amene Ambuye amuyenereza." (2 Akorinto 10:18)

Akatswiri a nzeru za Agiriki ankalipiritsa ndalama zambiri ophunzira amene ankafuna kuphunzira kuchokera kwa iwo. Kuti akope ophunzira ameneawa, iwo ankadzitamandira ndi chidziwitso chawo, udindo wawo pagulu la anthu, kapena anthu otchuka omwe ankawadziwa ndi kuwalemekeza. Izi ndi zomwe ankachitanso aphunzitsi onyenga omwe analowa mumpingo wa ku Korinto (2 Akorinto 10:12; 11:19-20).




Koma Paulo sankalipiritsa ndalama chifukwa chophunzitsa ena zimene ankadziwa, sankapereka makalata omuyamikira, ndiponso sankadzitamandira. Ndipo chifukwa cha zimenezi, anthu ena ankamunyoza! Kodi akanadziteteza bwanji?

Zinkaoneka ngati Paulo ankafunika kuyamikiridwa pamaso pa Akorinto kuti amulandire. Koma sanali iye amene anayenera kudzitamandira yekha (Miyambo 27:2). Paulo analola kuti Mulungu akhale amene amuyamikire (2 Akorinto 10:18)

Ngati pali chinthu chimene tingadzitamandire nacho kapena kudzikwedza nacho, ndiko kumudziwa Mulungu ndi kumumvera lye (Yer. 9:24; 2 Akor. 10:17).





**M'MENE TINGACHIRE
NDI APHUNZITSI
ONYENGA**

ONYENGA ODZIYESA ATUMWI

**"Pakuti anthu oterewa ndi atumwi onama, antchito achinyengo, odzizimbayitsa ngati atumwi a Khristu."
(2 Akorinto 11:13)**




Paulo amafuna kupereka mpingo woyera kwa Khristu (2 Akorinto 11:2). Koma mpingo unali pachiwopsezo chonyengedwa monga Hava, ndi kusiya kukhala mkwatibwi wa Yesu (2 Akorinto 11:3).

Kodi chiopsezo chenichenicho chinali chiyani? Ayuda amene ankadzitcha "atumwi akulu" a Yesu anafika ku Korinto, akuphunzitsa za "Yesu wina," "mzimu wina," ndi "uthenga wabwino wina" (2 Akorinto 11:4-5; Agalatiya 1:8).

Ngati munthu akulalikira za Yesu sikutanthauza kuti akutionetsera Yesu weniweni, monga momwe amafotokozedwera m'Baibulo. Mawu awo akhoza kukhala okongola, koma Satana mwiniwakeyo amadziwanso kulankhula zinthu zodabwitsa komanso kudziwonetsa ngati "mngelo wa kuunika" (2 Akorinto 11:14).

Kudzera muzochita komanso mawu awo, aphunzitsi wona amaphunzitsa "choonadi cha Khristu" (2 Akorinto 11:9-10). Koma aphunzitsi onyenga, amene amangonamizira kuti ndi opembedza, ndi atumiki achinyengo onamizira ngati atumwi (2 Akorinto 11:13-15).



PAULO NDI APHUNZITSI ONYENGA

"Kodi iwo ndi Ahebri? Inenso ndine Mhebri. Kodi iwo ndi Aisraeli? Inenso ndine Mwisraeli. Kodi iwo ndi zidzukulu za Abrahamu? Inenso ndine mdzukulu wa Abrahamu. " (2 Akorinto 11:22)



Kodi panali kufanana kotani pakati pa Paulo ndi aphunzitsi onyenga? Onse anali Ayuda amene analowa Chikristu (2 Akorinto 11:22).

Kodi panali kusiyana kotani pakati pawo? Apa Paulo akuyamba kulankhula ngati wamisala: "Kodi iwo ndi atumiki a Khristu? (Ndachita misala polankhula motere) ndawaposa " (2 Akorinto 11:23). Ngati enawo ankadzitamandira kuti anavutika chifukwa cha Khristu, Paulo anali ndi umboni wochuluka kwambiri: anakwapulidwa; anaikidwa m'ndende; anakumana ndi chiopsezo cha imfa; anaponyedwa miyala; ngalawa zinamusweka panyanja; anakumana ndi zoopsa za mitundu yonse; anamva njala, ludzu, kuzizira, ndi kusowa zovala; ndipo nthawi zonse ankadera nkhawa mipingo (2 Akorinto 11:23b-29).

Ndipo apa ndi pamene "kupenga" kwa Paulo kumathera. Iye sanafune kupereka chithunzi chakuti ankafuna kudzitamandira chifukwa cha zimene anachitira Khristu. Kudzitamandira kwake kwenikweni (kapena ulemmerero wake) kunali pa zimene Khristu anamuchitira.


Mphamvu yake yeniyeni inali mu kufooka kwake, kumene kunamutsogolera kudalira Yesu kotheratu(2 Akorinto 11:30-31; 12:6-10).



KUDZIYESA NDI KUPAMBANA

"Tadzisanthulani nokha kuti muone ngati muli m'chikhulupiriro; dziyeseni nokha. Kodi simuzindikira kuti Khristu Yesu ali mwa inu, ngati si choncho mwalephera mayesowa?" (2 Akorinto 13:5)

Nthawi imene Paulo ankayenera kupita ku Korinto inali kuyandikira. Kodi akakumana ndi chiyani, ndipo anayenera kuchita zotani potengera zimenezo? (2 Akorinto 13:1-2).



Paulo anali wokonzeka kugwiritsa ntchito chilango cha mpingo mwamphamvu: kubwezeretsa olapa, ndi kulanga ouma mtima.

Ankaopa kuti akafika, akawapeza ali m'mikangano ndi m'machimo osiyanasiyana. Ankaopa kuti angadzafunike kulirira ochimwa amene sanalape (2 Akorinto 12:20-21).

Choncho, nthawi imeneyo isanafike, Akorinto anayenera kuganizira mozama ndi kudzifufuza okha (2 Akorinto 13:5).

Paulo, kumbali yake, anawapempherera kuti asiye kuchita zoipa, ayambe kuchita zabwino, ndi kuti akhale angwiro (2 Akorinto 13:7-9).



“Anthu a Mulungu akuwatsogolera ku Malemba Opatulika monga chitetezo chawo ku chikoka cha aphunzitsi onyenga ndi mphamvu zachinyengo za mizimu ya mdima. Satana amagwiritsa ntchito njira iliyonse imene angathe pofuna kulepheretsa anthu kudziwa Baibulo; pakuti mawu ake osavuta amavumbula chinyengo chake. Nthawi iliyonse ntchito ya Mulungu ikatsitsimutsa mtima, kalonga wa zoipa amadzuka ndi kugwira ntchito mwamphamvu kwambiri; tsopano akuyika pamodzi khama lake lalikulu pofuna kulimbana komaliza ndi Khristu ndi otsatira Ake. [...] Chinyengochi chidzafanana kwambiri ndi choonadi ndipo kudzakhala kosatheka kuzisiyanitsa popanda kugwiritsa ntchito Malemba Opatulika. Kudzera mu umboni wa Malemba, mawu aliwonse ndi chozizwitsa chilichonse ziyenera kuyesedwa.”